

LESSON 46

REDUPLICATION

The repetition of the stem in Adjectives generally corresponds to a superlative and expresses intensity : p. 55, 83

Antku ambirimбири very numerous	Milandu yankhaninkhani numerous
Nyumba yaikulukulu	Chingwe chachitalitali
Kamwana kakang'onong'ono	Zobvala zazifupifupi
Nyumba yosesasesa well swept	Nyimbo zosiyanasiyana various
Nsaru yakuthaitha worn out	Mpeni wakuthwaithwa very sharp
Njinga yakufaifa	Nyama yophikaphika.

With verbs, it expresses frequency or continuity :

Tinabvinabvina mpaka usiku.	Mwanayu amangoliralira.
Anawerengaawerenga kalata ija.	Ndikufunafuna kalata yake.
Amadzapemphapempha ndalama.	Amangolongololalongolola.
Nditakhalakhala pa khomo, mfumu anandiitana.	
Munali kuti? — Timadyaidya mtedza pakhomo apo.	

With Adverbs, it indicates intensity :

Konzani msangamsanga! quickly	Anachita daladala intentionally
Pang'onopang'ono very little	Pang'onopang'ono little by little
Msika uli pafupifupi very near	Ntchito yapatalitali very difficult
Kalekale long ago : Anamwalira kalekale, inu musanabadwe.	
Kalekale soon : Anathamanga kwambiri, kalekale wafika.	
Muziyendetsa njinga bwinobwino gently p. 69	Mwapolepole slowly
Anafotokoza nkhan mwa tsatanetsatane point by point	

With nouns : Akuluakulu elders, important persons

Anabzala mitengo ya mitundumitundu. of various kinds	
Chithunzithunzi picture	Mamvaimva rumours
Chimasomaso seduction	Munthu wa magwiragwira thief
Ndipatseni matambala okhaokha. only pennies p. 60	
Amagona wina pa yekha, wina pa yekha. separately p. 60	
Alliyense akhale ndi bukhu lakelake. his own book p. 34	
Tiuzeni chenicheni! something clear. p. 57	
Pakati penipeni right in the middle. Kwenikweni akufuna chiyani?	
Ponseponse : Konsekonse : Monsemonse everywhere p. 59	
Uku ndi uku here and there. Kwina ndi kwina in the differnt places	
Kambirimbiri often (: kawirikawiri). Tsiku ndi tsiku day by day	
Kale mazira mtengo wake unali khobidikhobidi (: limodzi khobidi)	
Ndinamva zakutizakuti p. 91 Mungathe kuyenda kwakutikwakuti.	
Phokoso linanka likulirakulira p. 81 Madzi ananka nacheperachepera.	
Reduplication is also found in Ideophones p. 98 Chetechete!	

INTERROGATIONS Here are a few words which are sometimes included in interrogations or exclamations :

Kodi...? just introduces a question : **Kodi mwabwera ndi mawu?**
It can also be an interjection of surprise **Kodi!** p. 15

Bwanji...? "Why?" **Bwanji simulankhula mawu?** How is it that you do not.
"How" **Muli bwanji?** **Mlandu wake unatha bwanji?**

Nanga...? "And what about...? **Iwo adya kale; nanga inu? (: kaya inu?)**
Njinga iyi ndi ya mphunzitsi; nanga iyo?
"by the way", "well **Muli bwanji nanga (:tsono)**
Mukupita kuti nanga? Choncho! Titani nanga?
"naturally, of course" **Inunso mukupita nawo?—Nanga!**
Ifenso tiyenera kuphunzira chizungu. Nanga! Why not?

Kani...? shows surprise in presence of something unexpected: "Is that so?"
Kani anakhoza mayeso!...Really? he did succeed.
Kani amatero! Muli pano kani! Ine ndimati munachoka.

Monga ntamfunsira mbeta, mungalole kodi? (:...nditamfunsira)
that..." the answer is expected to be positive; but in fact it may be negative. **Monga mvula ibwera lero?**
Monga mwakhoza mayeso? Monga mupitadi kuulendo?
Sometimes with the infix -ta-, it indicates a supposition:
Monga ntamfunsira mbeta, mungalore kodi? (:...nditamfunsira)

Ngati? expresses a doubt "Do you think that...?; it suggests that the answers will be negative:
answer will be negative.
Mwanayu amapita kusukulu ngati? Iyayi, amangokhala.
Akupita kuti, kuntchito ngati? Iyayi koma ku mowa.
Analankhula mawu ngati? Iyayi, anangoti chete.

Eti! (: Atil!) "Isn't it?" "Don't you?" p. 45; 90

Mwakongwa eti! Mukabwerenso mawa eti!

Nanji ! "so much the more" "a fortiori": **Nyumba iyi njabwino; nanji iyo!**
Amabvuta mkazi wake masiku onse. Nanji atakhuta mowa!

Malinga can be considered as a conjunction; it has two meanings :
"provided; if" **Ungathe kulowa nawo malinga ndiwe mkhristu.**
Ndigula njinga chaka chino malinga ndikapeza ndalama.
Adziwa Chichewa msanga malinga akamachita khama.
"according to", "in proportion to" **malinga ndi m'mene.**
Ndidzakulipirani malinga ndi m'mene mwagwirira ntchito.
Malinga ndi m'mene amasimbira alendowa, kwao kulibe nvula.

Cholinga "aim intention" **Anabwera ndi cholinga choti atenge mwanayo.**

Proverb : Mutu umodzi susenza denga.